## KODI MUNGACHITE CHIYANI?

### Ngati mwazunzidwa:

**Kadandauleni:**

Kadandauleni za zomwe mwakumana nazozo kwa anthu oyenera, atsogoleri am'madera, mabungwe oyang'anira za ufulu wa anthu.

**Zina mwa zitsanzo za mabungwewa ndi;**

1. The Malawi Human Rights Commission (MHRC)
2. The Malawi Legal Aid Bureau
3. Centre for the Development of People (CEDEP)
4. The office of the Ombudsman
5. The independent complaints Commission
6. Centre for Human Rights Education and Assistance (CHREA)
7. Centre for Human Rights and Rehabilitation (CHRR)

**Kapezeni thandizo**

Muli ndi ufulu olandira chithandizo cha kuchipatala komanso uphungu pa nkhawa zomwe muli nazo kuti muchire. Chithandizochi mungachipeze ku maofesi olandira anthu nthawi zonse a CEDEP omwe akupezeka ku Hilltop mumzinda wa Mzuzu, Area 47 sector 5 mu mzinda wa Lilongwe; Mangochi Boma ku Mangochi ndi ku Nyambadwe DIC mu mzinda wa Blantyre, komanso ku chipatala chilichonse chomwe mwayandikana nacho.

### Ngati Mnzanu wazunzidwa:

**Muvetsereni:**

Mvetserani dandaulo lake (ngati akufuna kufotokoza) ndikukhala munthu yemwe atha kukumasukira (kumumvetsera mosaweruza)

**Muthandizeni kupeza thandizo:**

Muthandizeni kupita kwa anthu oyenerera kapena mabungwe omwe angathandize

**Yankhulani ndipo perekani thandizo:**

Kuyankhulapo ndi kuchita mgwirizano pothana ndi mchitidwe wozunzana zitha kuthandiza kuthetsa mchitidwewu.

## NDANI ANGAKUTHANDIZENI?

Bungwe la **Centre for Development Of People (CEDEP).** Bungweli limaika chidwi poteteza magulu omwe ali pachiopsezo chozunzidwa kuphatikizapo a m'gulu la LGBTIQ+.

P.O. Box 3251,
Lilongwe.
Cell: +265 884 282 072
Email: vzgambo@cedepmwi.org



# KUMVETSETSA KUNZUNZIKA KWA ANTHU A M'GULU LA LGBTIQ+

REDRESS
Ending torture, seeking justice for survivors

## KODI KUZUNZA N'CHIYANI?

Kuzunza ndi pamene wina wachititsa mzake kukhala ndi ululu wa m'malingaliro komanso pathupi mwadala. Zitha kuchitidwa ndi munthu wa udindo kapena anthu a m'dera omwe zochita zawozi zikudziwidwa kapena kuthandizidwa ndi Adindo a m'boma.

Kawirikawiri zimachitidwa pofuna kulanga, kuopseza kapena Kukakamiza munthu kuulula uthenga wina wake. Ithanso kukhala njira yosalira anthu a m'gulu la LGBTIQ+ chifukwa cha m'mene alili – chifukwa cha anthu omwe amakhala nawo chilakolako kapena kudzidziwa kuti ndi aamuna, aakazi kapena osintha.

**Zitsanzo zina ndi zotsatirazi;**

- **Ululu pathupi;** kumangidwa mwa nkhaza, kumenyedwa, nkhaza zokhudzana ndi kugonana, ndi njira zina zozunzira
- **Ululu m'malingaliro;** kuopsezedwa, kuyalutsidwa ndi kusalidwa
- **Kutchinjirizidwa pa zachuma;** kuopsezedwa, kuyalutsidwa kapena kusalidwa komwe kumakhuza kapezedwe ka chuma kapena mwayi osiyanasiyana pa chuma.

## UFULU WANU NGATI OZUNZIDWA

**Thandizo lakuchipatala:**

Muli ndi ufulu olandira thandizo chithandizo chakuchipatala komanso kulandira uphungu pa nkhawa zomwe muli nazo.

**Mwayi oyimiririrdwa pa mlandu:**

Muli ndi mwayi okhala ndi munthu okuimirirani pa mlandu kuti akuthandizeni ngati n'kofunika.

**Chilungamo :**

Muli ndi ufulu osuma kwa anthu oyenerera kuti mlandu wanu ufufuzidwe

**Chitetezo:**

Muli ndi ufulu otetezedwa ku mazunzo ena pamene mukuyendetsa mlandu wanu.

**Chipepeso:**

Mutha kulandira chipepeso komanso zinthu zina pofuna kukonza mazunzo omwe munalandira

**Umembala:**

Mutha kukhala nawo pazochitika zilizonse zakumtima kwanu.

## MALAMULO

Dziko la Malawi lili ndi udindo woletsa komanso wopewa kuzunzana kwa anthu. Adindo akuyenera kufufuza zokhudza kuzunzana, ndi kuzenga mlandu ochita mchitidwe oterewa. Adindo akuyeneranso kuthandiza komanso kuteteza ochitiridwa izi, ndipo aonetse kuti anthuwa alandira chipepeso.

**Malamulo a m'Malawi**

- Chiletso cha m'malamulo oyendetsera dziko; Amaletsa kuzunzana komanso kuchitira nkhaza ena (Gawo 19 (3))
- Palibe kuloleza kuzunza: Lamuloli sililoleza kuzunza ena pa nthawi ina iliyonse ( Gawo 44 ndi 45 (2) (b) malamulo oyendetsera dziko)
- Chitetezo kwa oganiziridwa mlandu: Ngakhale malamulowa sakamba za kuzunza ena, anthu ochitira nkhanza anzawo atha kuzengedwa pa milandu ina malingana ndi malamulowa.

**Malamulo a Mayiko onse**

- Mgwirizano wa mayiko onse pothana ndi kuzunza ena wotchedwa the UN concention against torture (UNCAT). Mgwirizanowu ukupereka mphamvu ku dziko la Malawi kupewa komanso kuchitapo kanthu munthu akazunzidwa.
- Mgwirizano wa m'mayiko amu Africa okhudza ufulu wachibadwidwe wa anthu otchedwa The African Charter on Human and Peoples Rights (ACHPR). Malamulowa akupereka mphamvu ku dziko la Malawi kuti liletse komanso kupewa kuzunza ena.